# NKHAMENYA ZONE EXAMINATION BOARD

## 2025 PRE-ZONAL MOCK T3

## CHICHEWA (100 MARKS)

## STANDARD 6

**NAME OF A LEARNER:** ______________________________ **DATE** ____________

**NAME OF SCHOOL:** ______________________________

**GAWO A (MALIKISI 30)**

**Langizo**: yankhani funso limodzi lokha mwamafunso awiri ali m'musiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo chanu pa mutu uwu "**Ulendo wosaiwalika".** Mwazina tsatani izi.

   **Ndime Yoyamba**
   - Tsiku lomwe ulendo udachitika
   - Komwe mudapita
   - Amene mudapita nawo
   - Cholinga cha ulendowo

   **Ndime Yachiwiri**
   - Tchulani zinthu ziwiri zomwe mudachita
   - Fotokozani kufunika kwa ulendowo

   **Ndime Yachitatu**
   - N'chifukwa chiyani ulendowo udali wosaiwalika?

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa mnzanu yomufotokozera za m'chitidwe owononga katundu wa pasukulu panu. Mwazina tsatani izi polemba.

   **Ndime Yoyamba**
   - Katundu yemwe ali pasukulu panu
   - Momwe sukulu yanu idamupezera katunduyo.
   - Omwe amaononga katunduyo

   **Ndime Yachiwiri**
   - Zomwe zimachititsa kuononga katunduyo.
   - Kuipa kwa mchitidwe owononga katundu wa pasukulu.

   **Ndime Yachitatu**
   - Momwe mungasamalire katundu wa pasukulu panu.

______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## GAWO B (MALIKISI 20)

## KUMVETSA NKHANI

- Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo pamizere ili pansi pa funso lililonse.

Atadzidabwa Milika, yemwe adali Chisamba cha banja la a Msumba, adauza amnzake omwe amacheza nawo. Pakuti ena mwa amnzakewo adali ndi mantha sadadziwe chinachilichonse choti angamulangize m'nzawoyo. Pagululi padali anamwali atatu omwe atamva zimene Milika ananena adangotsizinirana. Adachita izi podziwa kuti bongololo sadzolera mafuta pagulu makamaka sadafune kulawura amene adali asanagwe m'dothi–pansi pamtima atsikanawo adadziwa kuti tsopano Milika ndi namwali mzawo. Mmene zimachitika zonsezi n'kuti atsikanawo akuchokera ku madimba atadendekera madengu ndipo ena nsengwa za ndiwo zoti akadyere nkhomaliro.

Atsikana akuluakulu aja sadanene chilichonse pankhaniyo pakuti idali nkhani yofunika ntchembere. Omwe samadziwa kanthu amangomuseka Milika pakuti kwa iwo chilichonse chidali chachilendo. Mauthuwo adali Sekelani, Nachanza ndi Elube. Enawo adali Tionge ndi Mtupa. Onse adali atsikana a m'mudzi mwa mbale. Mudziwu umatchuka ndi gule wa chintali. Atafika kumudzi, anamwali aja adadziwitsa amayi ake a Milika. Nthawi yomweyo amakewo adatengera nkhaniyo kwa namkungwi. Atamva izi namkungwiyo sadafune kuchedwa. Iye adauza ntchembere gandule zapamudziwo. Ntchembere gandulezo zidatsinana makutu ndipo zidagwirizana zokhala naye pansi mtsikanayo. Kutacha adamutuma Milika kuti akumane naye m'kanyumba komata.


Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**mafunso**

A. Tchulani mudzi umene Milika amakhala (1 maliki)

______________________________

B. Perekani mayina awiri a anthu m'nkhaniyi (2 malikisi)

______________________________

C. Nchifukwa chiyani Milika adauza anzake? (2 malikisi)

______________________________

______________________________

D. Kodi anamwali adachitanji atamva nkhani ya Milika? (2 malikisi)

______________________________

E. Pezani mawu otsutsana mmatanthauzo ndi awa:
   i) Chitsitsansepe ______________________________ (1 maliki)
   ii) Mnyamata ______________________________ (1 maliki)

F. Perekani chifukwa chimodzi chomwe atsikana atatu atamva adangotsinzinirana (2 malikisi)

______________________________

G. Mukadakhala ndinu mayi a Milika mukadatani (2 malikisi)

______________________________

H. Kodi mudziwu umatchuka ndi gule wanji (1 maliki)

______________________________

I. Perekani mawu ofanana mmatanthauzo ndi awa (2 malikisi)
   i) Kugwa mdothi ______________________________
   ii) Poduka mphepo ______________________________

J. N'chifukwa chiyani ntchembere gandule zidatsinana makutu (2 malikisi)

______________________________

K. Perekani mutu oyenera wa nkhaniyi (2 malikisi)

______________________________

## GAWO C (10 MALIKISI)

**Werengani kankhanika mosamala ndipo muyankhe mafunso mosamala.**

"Abambo ndi anyamata, tonse mawa tikumane kwa mfumu. Tikatenge mikondo, mipaliro, mauta ndi zibonga m'manja. Aliyense pobwera kumeneko, mwendo wa nyama akapereke kwa mfumu ngati nsembe".

**MAFUNSO**

A. i) Tchulani mtundu wa malonje. (1 maliki)

______________________________

ii) Ndani akupereka malonjewa (1 maliki)

______________________________

B. Tchulani ubwino ovala yuunifolomu pa sukulu (1 maliki)

______________________________

C. Perekani njira ziwiri zomwe mungasamalire mabuku (2 malikisi)

______________________________

______________________________

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

A. chipanda

______________________________

B. kwa

______________________________

C. mbwee

______________________________


Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

D. mofulumira

E. yabwa

## GAWO D (40 MALIKISI)

Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m'mafunso awa:

**Mafunso 6 mpaka 10: Sankhani mitundu ya mawu amene atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

6. **Wanga** adathawa dzulo.
   - A. dzina
   - B. mneni
   - C. mlowammalo
   - D. mfotokozi
7. Mbuzi zimakonda msipu **wobiriwira**.
   - A. mfuwu
   - B. muonjezi
   - C. mneni
   - D. mfotokozi
8. Atangofika, **khwimbi** lonse lidaimirira.
   - A. Dzina
   - B. muonjezi
   - C. mlowam'malo
   - D. mfuwu
9. Mayi wina adali **wefuwefu** kuthamangira kwa iye
   - A. mfuwu
   - B. mperekezi
   - C. mvekero
   - D. Dzina
10. **Poti** wandipempha ndikupatsa.
    - A. mperekezi
    - B. mlumikizi
    - C. mfotokozi
    - D. Muonjezi

**Mafunso 11 mpaka 15: Sankhani mitundu ya alowammalo omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

11. **Awo** akupita kwawo.
    - A. wochuluka
    - B. wamwini
    - C. woloza
    - D. wofunsa
12. **Amene** sakufuna asalembe.
    - A. wagwirizano
    - B. waumwini
    - C. wofunsa
    - D. woloza
13. Ndagula **ziwiri** zokha.
    - A. wochuluka
    - B. wofunsa
    - C. owerenga
    - D. waumwini
14. **Zathu** zalowa mkhola.
    - A. waumwini
    - B. wofunsa
    - C. wochuluka
    - D. wapafupi
15. **Ena** alemba kale zabodza.
    - A. wamgwrizano
    - B. woloza
    - C. wopatula
    - D. wofunsa

**Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani mitundu ya mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

16. **Mwayi** akulemba mayeso
    - A. lopanda mwinimwini
    - B. la unyinji
    - C. lamwinimwini
    - D. la chinthu chokhuzika
17. Iye walowetsa **m'sambi** wa nkhosa m'khola
    - A. La unyinji
    - B. la chinthu chosakhudzika
    - C. lopanda mwinimwini
    - D. lachinthu chokhudzika
18. Munthuyu alibe **mtendere** muntima mwake
    - A. lopanda mwinimwini
    - B. lachinthu chokhudzika
    - C. la mwinimwini
    - D. lachinthu chosakhudzika
19. **Nyani** wadya chimanga chija.
    - A. la mwinimwini
    - B. lopanda mwinimwini
    - C. la unyinji
    - D. lachinthu chokhudzika
20. Iye wandigenda ndi **mwala** uwu.
    - A. lachinthu chosakhudzika
    - B. la mwinimwini
    - C. lachinthu chokhudzika
    - D. la unyinji

**Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani mawu ofanana mmatanthauzo ndi mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

21. Iye ndi **njinga**.
    - A. wachimasomaso
    - B. wofatsa
    - C. waulemu
    - D. wachinsinsi
22. Adatha **zilumika** ziwiri alibe mwana.
    - A. masiku
    - B. miyezi
    - C. zipika
    - D. zaka
23. Maliya adali **mzime** m'banja lathu.
    - A. wamkulu
    - B. chitsitsamsepe
    - C. womaliza
    - D. chisamba
24. Namulangeni adakatola nkhuni **kudondo**.
    - A. phiri
    - C. chipululu


Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

B. Dambo D. Nkhalango

25. Atate adakhala pa **chikumba**.
    A. mphasa C. mkeka
    B. chikopa D. pansi

**Mafunso 26 mpaka 30: Sankhani matanthauzo a Zilape zotsatirazi**

26. Mbalame yaikira pa minga
    A. Lilime C. mphuno
    B. chisa D. mpira
27. Ndodo ya amfumu siiwongoleka.
    A. chipululu C. mbatata
    B. Nyanja D. msampha
28. Mbalame ziwiri zaoloka Nyanja.
    A. dzungu C. dziko
    B. maso D. mlengalenga
29. Chimunda change chachikulu koma pokolola Mkumanja.
    A. Bwenje C. masamba
    B. Udzu D. Tsitsi
30. Zungulira uku tikumane uko.
    A. Lamba C. maso
    B. makutu D. chithunzithunzi

**Mafunso 31 mpaka 35: Sankhani magulu amayina omwe mwapatsidwa.**

31. Dzina
    A. Li – Ma C. U – Ma
    B. Ka – Ti D. I – Zi
32. Mlendo.
    A. Mu – A C. Li – Ma
    B. U – Ma D. Mu – Mi
33. Tiana
    A. Li – Ma C. U – Ma
    B. Ka – Ti D. Chi – Zi
34. Ulalo
    A. Li – Ma C. U – Ma
    B. I – Zi D. Mu – Mi
35. Ngolo
    A. Mu – Mi C. Chi – Zi
    B. Ka – Ti D. I – Zi

**Mafunso 36 mpaka 40: Sankhani chachikazi cha mayina otsatirawa.**

**36. Ndoda**
    A. chemvali C. Azakhali
    B. Ntchembere D. mpongozi
37. Chipsolopsolo
    A. mwanapiye C. thadzi
    B. Tambala D. msoti
38. Muphwa
    A. mfumukazi C. nkhosa
    B. mulolokazi D. thadzi
39. Phungu
    A. zakhali C. Namkungwi
    B. mpongozi D. Nkota
40. Mzambwe.
    A. thadzi C. Nkhunda
    B. mkota D. msoti

**Mafunso 41 – 45: Sankhani mawu otsutsana mmatanthauzo ndi mau omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zitsatirazi.**

41. **Makedzana** anthu amakonola mu mtondo.
    A. kale C. mkucha
    B. makono D. m'bandakucha
42. Msipu siusowa nyengo **yadzinja**.
    A. Ng'amba C. chisanu
    B. mvula D. mwavu
43. Abambo **amasula** mbuzi ija.
    A. Amanga C. alasa
    B. akwizinga D. atulutsa
44. Galimoto yagwera **kuchigwa**.
    A. Dera C. manda
    B. Gomo D. mtsinje
45. M'phwawo ananyamuka **kutacha**.
    A. kukuyera C. kutada
    B. mvula isabwere D. kutayera

*MAFUNSO ATHERA PANO!!!!*


Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com